# TIYENI TIDZIWE ZA SABATA

***Pofuna kumveketsa bwino, mmaphunziro athu onse timagwiritsa ntchito maina enieni ACHIHEBERI a mulengi wathu YAHWEH malo mwa maina aulemu monga Mulungu ,Ambuye, komanso tikugwiritsa ntchito dzina la mwana wake wobadwa yekha YAHUSHA Mmalo mwa dzina loti Yesu lomwe lilibe tanthauzo mu Chiheberi komano ndikumasulila kolakwika kochokera ku chigiriki.***

*Baibulo limaphunzitsa kuti tonsefe tiyenera kukhala ndi chikhulupiriro chimodzi. Tsopano tiyeni tione umodzi mu Sabata ngati chikhulupiriro chimodzi Cha m'Baibulo.*

**Aefeso 4:3-5,** ***3.ndi kusamalitsa kusunga umodzi wa Mzimu mwa chiimangiriro cha mtendere.***

***4 Thupi limodzi ndi Mzimu mmodzi, monganso anakuitanani m’chiyembekezo cimodzi ca maitanidwe anu;***

***5 Ambuye mmodzi, chikhulupiriro cimodzi, ubatizo umodzi,***

***1.KODI TINGATSATIRE CHIANI POFUNA KUDZIWA CIFUNIRO CHA YAHWEH?***

***Yesaya 8:20 kuchilamulo ndi ku umboni ngati iwo sanena malinga ndi mau awa, ndithu sadzaona m'banda kucha.***

***2Timoteo 3:16-17**,16* ***Lemba liri lonse adaliuzira Mulungu, ndipo lipindulitsa pachiphunzitso, chitsutsano, chikonzero, chilangizo ca m'chilungamo:***

***17 kuti munthu wa Mulungu akhale woyenera, wokonzeka kuchita nchito iri yonse yabwino***

***2.KODI SABATA LINAYAMBA LITI?***

***Genesis 2:2-3, "Tsiku lacisanu ndi ciwiri Yahuwah anamariza ntchito yonse anaipanga; ndipo anapuma tsiku lacisanu ndi ciwiri ku ntchito yake yonse.***

***3 Mulungu ndipo anadalitsa tsiku lacisanu ndi ciwiri, naliyeretsa limenelo: cifukwa limenelo adapuma ku nchito yake yonse imene Mulungu anailenga ndi kupanga"***

***GENESIS 26:5 Chifukwa kuti Abrahamu anamvera mau anga, nasunga chilangizo changa ndi maweruzo anga, ndi malemba anga ndi malamulo anga. KJV***

*Malamulo awa amene Abrahamu anasunga anaphatikizaponso Sabata – pamodzi ndi*

*malamulo ena onse amene anapatsidwa kwa Adamu.*

*Aka ndi koyamba kuti mawu oti "malamulo" agwiritsidwe ntchito mu Torah – ndi Abrahamu, izi ndi pafupifupi 1800 BC.*

*Eksodo 16:23 ndi Mose pafupifupi 1490 BC – pafupifupi zaka 300 pambuyo pa Abrahamu.*

***3.KODI SILINAYAMBA PAPHIRI LA SINAI NDI MOSE?***

*Eksodo 16:23 Ndipo ananena nao, Ichi ndi chomwe YAHWEH analankhula, Mawa ndiko kupuma, Sabata lopatulika la YAHWEH; chimene muziotcha, otchani, ndi chimene muziphika phikani; ndi chotsala chikukhalireni chosungika kufikira m'mawa.*

***4.KODI NDI CHIANI CHIMENE CHIKUONETSA SABATA KUTI NDI LOFUNIKA?***

***Mateyu 24:20 Ndipo pempherani kuti kuthawa kwanu kusakhale pa nyengo yachisanu, kapena pa Sabata;***

***5.KODI PAPHIRI LA SINAI LINABWERETSEDWA NGATI CHIANI?***

***Eksodo 20:8-12. "Uzikumbukila tsiku la Sabata, likhale lopatulika.***

***9.Masiku asanu ndi limodzi uzigwira, ndi kumariza nchito zako zonse;***

***10.koma tsiku lacisanu ndi chiwiri ndilo Sabata la YAHWEH Mulungu wako; usagwire nchito iri yonse, kapena iwe wekha……..***

***11.cifukwa masiku asanu ndi limodzi YAHWEH adamariza zakumwamba ndi zapansi, ndi nyanja, ndi zinthu zonse ziri m'menemo, napumula tsiku lachisanu ndi chiwiri; chifukwa chake YAHWEH anadalitsa tsiku la Sabata kuti likhale lopatulika.***

***6.KOMA KODI MALAMULO AWA SANATHERE PA MTANDA?***

***Mateyu 5:17 Musaganize kuti ndinadza Ine kudzapasula chilamulo kapena aneneri: sindinadza kupasula, koma kukwaniritsa.***

***18 Pakuti indetu ndinena kwa inu, Kufikira litapitirira thambo ndi dziko, kalemba kakang'ono kamodzi kapena kansonga kache kamodzi sikadzachoka kuchilamulo, kufikira zitakwanilitsidwa zonse***

***Chibvumbulutso 14:12 Pano pali cipiriro ca oyera mtima, cha iwo akusunga malamulo a Yahuwah, ndi chikhulupiriro cha Yahusha.***

***7.KODI SABATALI LIMATIKHUDZA BWANJI?***

***Ezekiel 20:12,20***

***, 12; Ndipo ndinawapatsanso masabata anga akhale chizindikilo pakati pa Ine ndi iwo, kuti adziwe kuti Ine ndine YAHWEH wakuwapatula.***

***20 muzipatulanso masabata anga, ndipo adzakhala chizindikilo pakati pa Ine ndi inu, kuti mudziwe kuti Ine ndine YAHWEH Mulungu wanu***

***8.NDI CHANI CIMENE CHIKUONETSA KUTI YAHWEH, AMAFUNA ANTHU AKE AZISUNGA SABATA?***

***Yesaya 56:6-7,***

***6.Alendonso amene adziphatika okha kwa YAHWEH, kuti amtumikire Iye, ndi kukonda dzina la YAHWEH, akhale atumiki ake, yense amene asunga sabata osaliipitsa, nagwira zolimba cipangano canga;***

***7. naonso ndidzanka nao ku phiri langa lopatulika, ndi kuwasangalatsa m'nyumba yanga yopemphereramo; zopereka zao zopsereza ndi nsembe zao zidzalandiridwa pa guwa la nsembe langa; pakuti nyumba yanga idzachedwa nyumba yopemphereramo anthu onse.***

***Nehemiah 13:18 Sanatero kodi makolo anu, ndipo Mulungu wathu anatifikitsira ife ndi mudzi uno coipa ichi chonse? Koma inu muonjezera Israyeli mkwiyo pakuipsa Sabata.***

***9.KODI MUCHIPANGANO CA TSOPANO AMASUNGA SABATA?***

***Luka 4:16 Ndipo (Yahusha) anadza ku Nazarete, kumene analeredwa; ndipo tsiku la Sabata analowa m'sunagoge, monga anazolowera, naimiriramo kuwerenga m'kalata.***

***Machitidwe 17:2 Ndipo Paulo, monga amacita, analowa kwa iwo; ndipo masabata atatu ananena ndi iwo za m'malembo, natanthauzira,***

***Machitidwe 18:4, Ndipo anafotokozera m'sunagoge masabata onse, nakopa Ayuda ndi Ahelene.***

***10.KOMA KODI SABATALI SILINALI TSIKU LA AYUDA?***

***Mariko 2:27-28 Ndipo ananena nao, Sabata linaikidwa chifukwa ca munthu, si munthu cifukwa cha Sabata;***

***28 motero Mwana wa munthu ali mwini dzuwa la Sabata lomwe.***

***Chibvumbulutso 1:10 Ndinagwidwa ndi Mzimu tsiku la Ambuye, ndipo ndinamva kumbuyo kwanga mau akuru, ngati a lipenga.***

***11KODI TSIKU LA AMBUYE NDI LITI?***

***Yesaya 58:13-14***

***12.KODI YAHUSHA ANATSUSANA NDI AYUDA CIFUKWA CHIANI PA ZAKUSUNGA SABATA?***

*Mateyu22:29, Koma Yahusha anayankha, nati kwa iwo, Mungolakwa osadziwa malembo, kapena mphamvu za Mulungu.*

***13.KODI MASIKU OMALIZA ANO TIYENERA KUSUNGANSO SABATA?***

***Mateyu 24:20-21 Ndipo pempherani kuti kuthawa kwanu kusakhale pa nyengo yacisanu, kapena pa Sabata;***

***21pakuti pomwepo padzakhala masauko akuru, monga sipadakhale otero kuyambira ciyambi ca dziko, kufikira tsopano, inde ndipo sipadzakhalanso.***

*Aheberi 4:6-9*

*6.Popeza tsono patsala kuti ena akalowa momwemo, ndi iwo amene Uthenga Wabwino unalalikidwa kwa iwo kale sanalowamo cifukwa ca kusamvera,...*

*7. Alangizanso tsiku lina, ndi kunena mu Davide, itapita thawi yaikulu, lero,monga zanenedwa kale,lero ngati mudzanva mawu ake musaumitse mitima yanu*

*8. Pakuti ngati Yoswa akadawapumitsa iwo sakadalakhula m`tsogolomo za tsiku lina*

*9.Momwemo utsalira mpumulo wa Sabata wa kwa anthu a Mulungu.*

***14.KODI NDIKOFUNIKIRA KUSUNGA SABATA KUTI TIKALOWE M'MOYO WOSATHA?***

***Mateyu 19:17 Ndipo Iye anati kwa iye, Undifunsiranji za cinthu chabwino? alipo Mmodzi ndiye wabwino: koma ngati ufuna kulowa m'moyo, sunga malamulo.***

***15.NANGA MUNTHU AKAYESA KUSUNGA MALAMULO ONSE KOMA SABATA LOKHA OSALISUNGA, KODI AZAPULUMUKA?***

***Yakobo 2:10-12,***

***10.Pakuti amene ali yense angasunge malamulo onse, koma akakhumudwa pa limodzi, iyeyu wacimwira onse.***

***11.Pakuti Iye wakuti, Usacite cigololo, anatinso, Usaphe. Ndipo ukapanda kucita cigololo, koma ukapha, wakhala wolakwira lamulo.***

***12.Lankhulani motero, ndipo citani motero, monga anthu amene adzaweruzidwa ndi lamulo la ufulu.***

***16.KODI NGATI NDIKUSUNGA SABATA NDIYE KUTI NDIDZAPULUMUKE?***

***Mateyu 7:21-23, 21. Si yense wakunena kwa Ine, Ambuye, Ambuye, adzalowa mu Ufumu wa Kumwamba; koma wakucitayo cifuniro ca Atate wanga wa Kumwamba.***

***22 Ambiri adzati kwa Ine tsiku lomwelo, Ambuye, Ambuye, kodi sitinanenera mau m'dzina lanu, ndi m'dzina lanunso kuturutsa***

*mizimu yoipa, ndi kucita m'dzina lanunso zamphamvu zambiri?*

*23pamenepo ndidzafukulira iwo, Sindinakudziwani inu nthawi zonse; cokani kwa Ine, inu akucita kusayeruzika*

*Mateyu 4:4Koma Iye anayankha nati, Kwalembedwa,Munthu sadzakhala ndi moyo ndi mkate wokha, koma ndi mau onse akuturuka m'kamwa mwa Mulungu.*

***17. KODI YAHUSHA ANANENA CHIYANI KWA IWO OSASUNGA SABATA?***

*Mateyu 15:8-9, 8 Anthu awa andilemekeza Ine ndi milomo yao; Koma mtima wao uli kutari ndi Ine.*

*9 Koma andilambira Ine kwacabe,Ndi kuphunzitsa maphunzitso, malangizo a anthu.*

*Yakobo 4: 17, Potero kwa iye amene adziwa kucita bwino, ndipo sacita, kwa iye kuli chimo.*

***18.NGATI ATSOGOLELI AKUTILAKWITSA NDIYE KUTI SITIKAPULUMUKA?***

*Mateyu 15:14 Kawalekeni iwo, ali atsogoleri akhungu. Ndipo ngati wakhungu amtsogolera wakhungu, onse awiri adzagwa m'mbuna.*

***Yesaya 9:16 Pakuti iwo amene atsogolera anthuwa, ndiwo awasokeretsa; ndipo iwo amene atsogoleredwa nao aononngeka.***

.

***19 NDIYE NDINGATANI INE?***

***Machitidwe 17:30-31, 30 Nthawi za kusadziwako Mulungu analekerera; koma tsopanotu alinkulamulira anthu onse ponse ponse atembenuke mtima;***

***31cifukwa anapangira tsiku limene adzaweruza dziko lokhalamo anthu m'cilungamo, ndi munthu amene anamuikiratu; napatsa anthu onse citsimikizo, pamene anamuukitsa iye kwa akufa.***

***Machitidwe 3:19-21, 19. Chifukwa chake lapani, bwererani kuti afafanizidwe macimo anu, kotero kuti zidze nyengo zakutsitsimutsa zocokera ku nkhope ya Ambuye;***

***20.ndipo atume amene anaikidwa kwa inu, Yahusha Mesiya;***

***21 amene thambo la kumwamba liyenera kumlandira kufikira nthawi zakukonzanso zinthu zonse, zimene Mulungu analankhula za izo m'kamwa mwa aneneri ake oyera ciyambire***

***20.NANGA NDINGAYAMBE LITI KUSUNGA ZIMENEZI?***

***Aheberi 3:7-8, 7. Momwemo, monga anena Mzimu Woyera Lero ngati mudzamva mau ake,***

***8. Musaumitse mitima yanu, monga m'kupsetsa mtimamo, Monga muja tsiku la ciyesero m'cipululu,***

***22. KODI NDINGATHE KUNGA SABATA?***

***Afilipi 4:13 Ndikhoza zonse mwa iye wondipatsa mphamvuyo.***

***2 Akorinto 3:5 si kuti tiri okwanira pa ife tokha, kuyesera kanthu monga mocokera mwa ife tokha; kukwanira kwathu kucokera kwa Yahweh***.

***Aheberi 7:25 kucokera komweko akhoza kupulumutsa konse konse iwo akuyandikira kwa Yahweh mwa iye, popeza ali nao moyo wace cikhalire wa kuwapembedzera iwo.***

***KODI POMALIZA MALAKI AKUTIKUMBUTSA CHIYAN?***

***Malaki 4:4-6;*** *4.Kumbukilani cilamulo ca Mose mtumiki wanga, ndinamlamuliraco m'Horebu cikhale ca Israyeli lonse, ndico malemba ndi maweruzo.*

*5.Taonani, ndidzakutumizirani Eliya mneneri lisanadze tsiku lalikuru ndi loopsa la YAHWEH.*

*6Ndipo adzabwezera mitima ya atate kwa ana, ndi mitima ya ana kwa atate ao; kuti ndisafike ndi kukantha dziko lionongeke.*

***Ngati mufuna kudziwa komanso kuphunzira zambiri zokhudza uthenga wa chipulumutso m'masiku ano otsiriza, Tipezeni pa***

***Study the Covenant calendar .com***

***https//:malawioutreach.teachery.co/***

***Kapena imbani foni pa manambala awa:***

- ***0881764072***
- ***0999856135***

***innocentrfbeula@gmail.com***